


MGONERO

 ...Ambuye. Ndipo ife ndithudi tikupepesa kuti tiribe mipando yoti anthu akhalepo, ndipo kwa iwo amene a—apititsidwa kutali, mpaka kunja. Ine ndangomva kumene, mphindi pang'ono zapitazo, kumene ife tikanakhala ndi malo a zisudzo mu New Albany, amene mwina mukanakhala anthu pafupifupi firii sauzande. Koma ife basi tinali basi... Chitsitsimutsochi chinali cha gulu laling'ono chabe kuno ku tchalitchi. Ndipo—ndipo ife ndi nthawi yaying'ono yobwera kunyumba. Ndipo ndife okondwa kwambiri kukuwonani inu nonse mutabwera.

² Ngati ine sindikulakwitsa, ine ndikumuwona m'bale wanga waku Georgia pano. M'bale, sindingathe kutchula dzina lanu pakali pano; Palmer, wochokera ku Macon, Georgia. Ndife okondwa kukhala nanu pano, M'bale Palmer.

M'bale Creech, kuno kutsogolo, ndife okondwa kukuwonani inu.

³ Ndipo ine ndikudziwa kuti penapake mchipinda muno muli Dokotala Lee Vayle, mmodzi wa othandizira a—a msonkhano ku Lima, Ohio, kumene ku...Iye ndi m'busa wa First Baptist church, ndi a—a bwenzi langalanga la ine. Iye anali kunyumba lero, ndipo wabwera kuti adzatichezere ife mu msonkhano. Ife mwinamwake, umodzi wa mausiku, ife tidzakhala naye iye kuti adzayime ndi kunena chinachake. Ine ndinayesetsa kuti ndimupangitse iye kuti atenge malo anga usikuuno, kuti ayankhule, ndipo wakana zimenezo. Chotero ife tikuyembekeza, mwinamwake, kuti mwina mawa usiku, kapena nthawiina, M'bale Vayle kapena ena a...adzakhoza kunena mawu amodzi kapena awiri, mwinamwake za zokhudza msonkhano kapena chinachake kumtunda uko, chirichonse chimene Ambuye angayike pa mtima wake.

⁴ Pali ena pano omwe ine ndikanakonda ndikanangotenga nthawi kuti ndiwazindikire iwo onse, koma ndife okondwa kuti inu muli pano. Ine ndikumuwona munthu mmodzi wamng'ono kumbuyo uko, yemwe ali gulu la atumiki amene amabwera, amene amadzandichezera ine masana ano, wochokera uko ku Arkansas komanso ku Missouri.

⁵ Ndipo tsopano, usikuuno, ife tikufuna tiyiwombole nthawi, chifukwa usiku uliwonse tidziyesera kuti tidzimaliza pofika naini koloko, ngati nkotheka. Usikuuno ndi usiku wa Mgonero, kotero zikhala mochedwerapo pang'ono usikuuno kuposa nthawizonse.

⁶ Mawa usiku, Ambuye akalola, ine ndikufuna ndidzalalikire pa: *Khalani Inu Chotero Angwiro* ndi *Nsembe Yangwiro*, mawa

usiku. Ndipo, kenako, limenero ndi pa Good Friday.

⁷ Ndipo kenako Loweruka usiku ndi *Kuyikidwa Mmanda*, ngati Ambuye alola.

⁸ Lamlungu m'mawa, msonkhano wa Kutuluka kwa dzuwa sikisi koloko. Ndipo pa teni koloko, msonkhano wa ubatizo. Ndipo hafu-pasiti teni, phunziro la Sande sukulu, la chiwukitsiro.

⁹ Ndipo Lamlungu usiku, msonkhano wa machiritso wa nthawi zonse monga ife timakhala nawo uko mu—mmunda wa uvangeli.

¹⁰ Chotero, tsopano ife tikudalira kuti inu muwabweretsa azimzanu ochimwa, ndi zina zotero, ndipo mubwera ndi kudzakhala nafe, ndi kudzatithandiza ife mu msonkhano uwu ukubwera . . . kupitiriza kwa msonkhano uno, kani.

¹¹ Ine ndiri ndi Baibulo latsopano, usikuuno, linapatsidwa kwa ine ndi wina, m'bale wachi Dunkard. Ndipo icho chiri ngati chinthu chachikulu. Ino ndi nthawi yoyamba imene ndayamba kulalikirapo kuchokera mmenemo. Ndi zovutirapo pang'ono kwa ine.

¹² Tsopano, ine ndikudziwa kuti ife takumana ndi cholinga chimodzi, icho ndi, ku—kudzapititsa patsogolo ntchito ya Khristu, ndi kudzapeza mtendere mmiyoyo yathu, ndi kudzatipanga ife kukhala amuna ndi akazi abwinoko, antchito abwinoko a Ambuye. Ndipo ngati ife tabwerera lingaliro lina lirilonse, bwanji, ndiye ife sitidalitsidwa ndi Ambuye. Ife tabwera kudzafuna thandizo. Ife tabwera, kudzamufunafuna Mulungu. Ndipo iyi ndi nyumba ya kukonza, kumene Mulungu amatipatsa ife madalitso Ake, ndi kudzatikonza ife ku zolakwa.

Tsopano basi ife tisanatsegule Mawu, kapena—kapena kupempha Mzimu Woyera kuti utithandize ife, tiyeni tiweramitse mitu yathu.

¹³ Atate Odala Akumwamba, mu Kukhalapo Kwanu Kwauzimu ife tikudzipereka tokha tsopano, ngati omvetsera ku Uthenga, ndi monga olankhula a Mawu; iduleni milomo imene ikuyankhula, ndi makutu amene ati amvetsera, ndi mitima imene iti ilandire. Ndipo mulole Mzimu Woyera ugawire kwa ife, usikuuno, ndi kupereka Choonadi cha chisomo Chamuyaya cha Mulungu, kwa aliyense wa ife; kuti, pamene ife tidzichoka mchipinda chino, usikuuno, ife tidzanene monga iwo amene ankabwera kuchokera ku Emau, “Kodi mitima yathu siinatenthe mkati mwathu, chifukwa Iye anayankhula nafe pa njira?” Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

¹⁴ Cha mu Bukhu la Uthenga wa Mateyu, mu mutu wa 26, ndime ya 27 ndi 28, kwa mutu ine ndikufuna kuti ndiwerenge.

Ndipo iye anatenga chikho, ndipo pamene iye anayamika, ndipo iye anapereka icho kwa iwo, ndipo anati, Imwani inu nonse;

Pakuti awa ndi magari anga a pangano latsopano, amene akhetsedwera ambiri kwa chikhululukiyo cha tchimo.

Koma ine ndinena kwa inu, ine sindidzamwa kuchokera pano za chipatso cha mpesa, mpaka tsiku limene ine ndidzamwa iwo mwatsopano ndi inu mu ufumu wa Atate anga.

¹⁵ Ndipo tsopano ife tiyankhula pa: *Mgonero*. Ndipo uwu ndi usiku wa *Mgonero* wapachiyambi.

¹⁶ Ndipo *mgonero* unachitika, poyamba, kumusi uko mu Igupto, *mgonero* woyamba, umene unali—mwanawankhosa wa paska amene anaphedwa, amene anali woyimira wa Khristu. Ndipo ambiri a ife tikuidziwa nkhani yakale yodala imeneyo, za momwe kuti iwo amene anadya *mgonero* kumusi uko, anayenda kudutsa mchipunulu kwa zaka forte. Ndipo pamene iwo anatuluka, panalibe mmodzi wofooka pakati pawo. Ndipo kumeneko, ngakhale zovala zawo sizinaperepeseke, kwa zaka forte Mulungu anali atawasunga iwo.

Ndi chitsimikizo chodala chotani icho chiri kwa ife usikuuno! Ngati icho chiri choyimira, ndiye Khristu ndi chenichenicho. Ndipo momwe Mulungu anapululumutsira ana!

¹⁷ Ndipo, mu kudya kwa *mgonero*, panali kusiyana pakati pa moyo ndi imfa. Iwo amene anali mkati, pansi pa magari okhetsedwa, anadya *mgonero*. Palibe amene akanakhoza kudya *mgonero* kunja kokhala pansi pa magari okhetsedwa. Magazi a mwanawankhosa anakhetsedwa poyamba, ndipo kenako anayikidwa pa mphuthu ndi pa chipupa cha chitseko... mphuthu ndi thabwa lopingasa, ndi pa chipupa cha chitseko. Ndipo kenako mwanawankhosa anawotchedwa, ndipo anali... ndipo—ndipo anadyedwa ndi masamba akhambi, ndipo iwo anadzimangirira okha. Magazi atatha kukhetsedwa, ndipo iwo anali atadutsa pansi pa magari okhetsedwa, iwo anali atadzimangirira mchiuno ndipo anali okonzekera kuti aziguba.

¹⁸ Ndipo tsopano ndi choyimira chokongola kwambiri usikuuno, cha, anthu amene amadya *Mgonero* sayeneranso kuyanjana kapena kugwirizana ndi zinthu za mdziko nkomwe. Iwo ayenera kubwera pansi pa Magazi choyamba, ndi kudzayeretsedwa ku tchimo lonse, limene liri kusakhulupirira, ndipo kenako nkuvekedwa ndi makonzekeredwe a Uthenga, atavala zida zonse za Mulungu, okonzekera kuyitanidwa nthawi iliyonse.

¹⁹ Ndipo icho chinali—chizindikiro chakuti mngelo wa imfa sakanakhoza kudutsa pansi pa magari amenewo. Mngelo wa imfayo ankayenera kudzuka ndi kupita pamwamba pa

magaziwo. Ndipo apo ndi pamene wolemba ndakatulo anapeza kudzodza, kwakuti, “Pamene Ine ndiwona Magaziwo, Ine ndidzadzutsa pa inu.”

Linali litayandikira ora la chiwombolo pamene iwo anavomereza mgonero, mwanawankhosa—wowotchedwa ndi—masamba omwe iwo anadya asananyamuke.

²⁰ Tsopano, mu choyimiridwa chimene ife tikuyenera kuyankhulapo, izo zinali zaka zambiri zapitazo, usikuuno, pamene Yesu anadya chimene ife timachidziwa monga Mgonero wa Ambuye, Mgonero. Ndipo pali chinachake cha izo, chimene, Iye anali woti akayankhula ndi ophunzira Ake. Ndipo asanachokeko, Iye ankafuna kuti akambirane ndi iwo za izo. Ndipo icho ndi. . . Iwo anali atakonzza chipinda. Iyo inali nthawi ya chiyanjano. Ndipo *mgonero* umatanthauza “chiyanjano.”

²¹ Mipingo yambiri imakhala ndi Mgonero wodzitsekera, ndiko kuti, zimakhala za mpingo wawo wokha pamene iwo akudya Mgonero wawo, koma kuno ife sindife chipembedzo, ife timakhala ndi Mgonero wotsegukira onse, pakuti ife timakhulupirira kuti wokhulupirira aliyense ali ndi ufulu ku gome la Ambuye, ndi kuyanjana mozungulira zinthu zabwino za Mulungu, ndi wokhulupirira aliyense, mosalabadira za kachikhulupiriro, mtundu, kapena chirichonse chimene iye angakhale, kuti onse anapangidwa kuti amwe mdalitso womwewo, Khristu.

²² Tsopano, ora lopambana ili linali litamuyandikira Ambuye wathu, imodzi mwa nthawi zoyesa kwambiri za ulendo Wake wonse wapadziko lapansi inali itayandikira. Nthawi yoyesa! Yesu ankayenera kudutsa mmayesero, chimodzimodzi basi monga momwe ife timadutsira mmayesero. Ndipo Baibulo linanena kuti, “Mwana aliyense amene amabwera kwa Mulungu ayenera kuyesedwa poyamba, kuphunzitsidwa, kukonzedwa.”

²³ Tsopano, anthu ambiri, chimakhala chiwonetsero pamene nthawi yamayesero ifika. Imakhala nthawi ya malo otsimikizira. Ndipo Baibulo linati, “Ngati ife sitingakhoze kupirira mayesero, ndiye ife timakhala ana apathengo,” ife timadzinenera kuti Mulungu ndi Atate wathu, ndipo komano Iye si Atate wathu. Pakuti ngati ife molondola, ndipo ndi mtima wathu wonse, tinawalandira Ambuye Yesu monga Mpulumutsi wathu, palibe kanthu pansi pano kapena mu mdima wonse wamuyaya kadzakhoze—kadzakhoze kutilekanitsa ife ku chikondi cha Mulungu chimene chiri mwa Khristu Yesu.

²⁴ Ine ndikudabwa mu tsiku lino, ndipo ndakhalapo nthawizonse pamene anthu amadzinenera kuti ndi Akhristu, ndipo, yesero laling’ono loyamba limabwera, iwo amagwera mmphepete mwa njira. Izo zimawonetsera kuti uko kunali kumvetsa kwaluntha kwa Khristu. Ndi chifukwa ambiri

samapirira lero, ndi chifukwa chakuti ndi kumvetsa kwaluntha. Mwaluntha, iwe ukhoza kukhulupirira Izo, koma Izo zimapitirira patsogolo kuposa zimenezo. Kumuvomereza Khristu, ndiko kumuvomereza Munthu wa Khristu.

²⁵ Ambiri a ife timavomereza chipembedzo cha Chikhristu pophonzira za kachikhulupiriro. Ena amavomereza Chikhristu pa ziphonzitso za ubatizo. Ena amakhulupirira kuti ndi Akhristu chifukwa cha kutengeka kwina kumene iwo anachita, monga kufuula, kapena kuvina mu Mzimu, kapena kuyankhula ndi malirime, kapena kukhala ndi mphatso yodabwitsa yoti apereke. Zinthu zonsezo ndi zabwino mmalo mwake. Koma, kumuvomereza Khristu, ndiko kumuvomereza Munthu wa Khristu, ndiyeno zinthu zinazi zimangogwera mu mzere.

²⁶ Tsopano, ngati Mulungu sanampatule Mwana Wake Yemwe ku mayesero ankhanza, ndiye Iye sadzakupatulani inu kapena ine ku mayesero ankhanza.

²⁷ Ndipo Yesu anali apa akukumanizana nalo yesero lalikulu kwambiri limene Iye anakhalapo nalo, Getsemene inayikidwa patsogolo pake basi, kumene yesero lokwanira kamodzi ndi kotsiriza lija likuyenera kubwera, [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi]. pamene zolemetsa za dziko lonse lapansi zinali pa phewa Lake lodala. Kunalibe wina aliyense Mmiyamba monse kapena dziko lapansi akanakhoza kuzipirira izo koma Iye. Ndipo kudziwa kuti machimo onse, machimo akale, ndi machimo atsopano, ndi machimo amtsogolo, anatsamira pa chigamulo ichi. Ndipo icho chinali chimodzi mwa zigonjetso zazikulu kwambiri zomwe Khristu anayamba wapambanapo, kapena kutsimikizira Umesiya Wake waukulu, monga pamene Iye ananena kwa Mulungu, “Si chifuniro Changa; Chanu chichitidwe.” Chimenecho chinali chigonjetso chachikulu chimene Iye anayamba wapambanapo. Ziwanza zonse zozunza zinali zitamuzungulira kuti zimupime Iye ndi kumuyesa Iye.

²⁸ Ndipo pamene ife tikonzana ndi Mulungu, mitima yathu ikakhala yangwirowo, ndipo Mzimu Woyera watenga malo Ake mu mtima mwathu, ndi chinthu chaulemelero kwambiri kuti tikhale ndi mayesero. Baibulo limatiuza ife kuti, “Mayesero athu ndi zoyesa ndi zamtengo wapatali kwa ife kuposa siliva ndi golide wa dziko lino lapansi.” Chotero, ife tiri, tikuyenera kukhala othokoza.

²⁹ Ine sindikufuna kuti ndidzibweretsemo ndekha mu zochitika zina, koma basi pamene izo zikubwera m’malingaliro mwanga, ine ndikukumbukira yesero lalikulu ndi lomaliza limene ine ndinali nalo la chondichitikira changa cha Chikhristu, kunali uko mu chipatala kunja kuno pa Spring Hill. Pamene, mkazi wanga anali atagona mnyumba ya mitembo kumusi kuno, mtembo, ndipo iye anali atangochoka kumene mmoyo uno, kuti akakhale ndi Mulungu. Ndipo zoyesa ndi mayesero zinali

zikuchitika! Osati basi winawake kumanena kuti, “Billy, ndiwe woyera wodzigudubuza.” Kapena, kumeneko sikunali kuyesedwa kochuluka. Ndipo mayesero ena aang’ono awa, ndi zina zotero, za kutsutsidwa ndi amuna amene ine ndimagwira nawo ntchito, iko sikunali kuyesedwa kochuluka. Koma ora langa lalikulu la yesero linadza pamene dokotala, Adair (zomwe ine ndinabwereza izo dzulo mu chipatala pamene ife tinakhala pamodzi), ndipo pamene iye anabwera kutsika mu holo kuti adzakumane nane, ndipo anandigwira ine pa dzanja, ndipo anati, “Billy, mwana wako akufa, ndipo palibepo mwayi kwa iye kuti angakhale moyo. Iye ali ndi chifuwa cha meninjaitisi.”

Ine ndinati, “Ndithudi ayi, adokotala!” Ndipo amayi ake atagona, mtembo!

³⁰ Ndipo ine ndinalowa mkati. Ndipo iye anati, “Tiyeko ndi ine.” Ndipo ife tinapita ku labotale, ndipo kumeneko iye anatenga kabotolo kakang’ono ka galasi, ndipo iye anakakhutchumula iko. Ndipo zinkawoneka kuti munali kophuka mmenemo. Iye anati, “Imeneyo ndi nyongolotsi ya meninjaitisi ndipo ili mwa mwanayo. Ife tinachotsa ichi kuchokera ku nsana, kuti tichotse kunjenjemerako.” Ndipo iye anati, “Mu ichi, ife takupeza kuti ndi chifuwa cha meninjaitisi.” Anati, “Iye anayamwira izo kuchokera kwa amayi ake.” Ndipo anati, “Ngati mwana ameneyo angakhale moyo, iye adzakhala wolumala, wosautsika. Koma,” iye anati, “mwa zifundo za Mulungu, mwanayo akakhala ndi amayi ake.”

Ine ndinati, “Adokotala, ine ndikufuna ndimuwone mwanayo.”

Iye anati, “Iwe sungakhoze kuchita zimenezo, Billy, chifukwa cha Billy Paul, mnyamata wako.” Anati, “Iwe ukhoza kutengera nyongolotsiyo kubwerera kwa iye.”

³¹ Ndipo, atatha kuyesera kundilimbikitsa ine mopambana momwe iye ankadziwira kuchitira kwake, pamene iye ankachoka mchipindamo, ine ndinazemba ndipo ndinapita kumusi mu chipinda chapansi. Ndipo pamene ine ndinakafika kumeneko, chipatala nthawi imeneyo sichinali chokonzedwa monga icho chikuchitira tsopano, ndipo zenera linali atalitsegula ndipo chophimba chinali chitachokapo, ndipo ntchentche zina zinali zitakalowa m’maso a mwana wamng’ono. Ndipo ine ndinaingitsa ntchentchezo ndipo ndinayang’ana pansu pa thupi lake laling’ono, lonse litakhwinyata, ndipo miyendo yake yaing’ono ikusunthira mmbuyo ndi mtsogolo. Ndipo ine ndinati kwa iye, “Sharry, wokonedwa, kodi iwe ukuwadziwa adadi?”

³² Ndipo izo zinkawoneka ngati kuti iye ankayesera kuti abayibitse dzanja lake laling’ono kwa ine; pafupifupi usinkhu wa miyezi eyiti kapena naini. Ndipo ine ndinayang’ana pa iye. Ndipo iye anali akuvutika kwambiri, mwana wamng’ono

wosalakwa, mpaka limodzi la diso lake laling'ono labuluu linatembuzika. Ululu wochuluka chomwecho! Oh, ine ndikanamulandira iye iwo nthawi iliyonse, mmalo mwa iye.

³³ Ndipo ine ndinagwada pansi pa mawondo anga, zitseko zitatsekedwa, ndipo ine ndinati, “O Mulungu, Atate, apo pagona mkazi wanga, mayi wa mwanayu wagona uko mnyumba yosungiramo mitembo. Apo pali Billy Paul pa bedi, akudwala. Ndipo apa pali mwana wanga, akufa. Inu ndithudi, Ambuye, simungamutenge iye. Ine ndimamukonda iye. Ndipo iye amafanana ndi amayi ake. Ine ndikufuna kuti ndimulere iye. Kodi Inu simutero chonde, O Mulungu, upulumutseni moyo wa mwana wanga?”

³⁴ Ndipo pamene ine ndinayang'ana mmwamba... Ndipo monga inu nonse mmadziwa, ine nthawizonse ndakhala ndikuwona masomphenya. Panawoneka ngati chinsalu chakuda chinayamba kufutukuka, chikutsikira pansi, ndipo ngati kuti Mulungu watenga pemphero langa ndi kuliponyera ilo mmbuyo momwe pa nkhope yanga. Ndipo ine ndinati, “Kodi ine ndachita chiyani, Mulungu? Kodi ine ndalakwira malamulo Anu, kuti ine ndilandire chilango ichi? Ngati ndi choncho, Inu mungondiwulurira izo, ndipo ine ndilapa. Ine ndichita chirichonse, koma musamutenge mwana wanga.” Ndipo ine ndinamuwona iye akupita, mulimonse. Ine ndinadzuka.

³⁵ Ndipo kenako woyesayo anabwera kwa ine. Imeneyo inali nthawi imodzi mmoyo wanga wonse, imene ine ndingakhoze kuyitchula, inali mphindi yovuta, Getsemane wanga. Pamene ine ndinali nditangogwirizira movutikira pa bedipo, mdierekezi anati, “Ndi zimenezotu. Imeneyo ndiyo mphotho yoyesera kumutumikira Iye. Iwe ukutanthauza kuti Iye angamutenge mayi wamng'ono wa zaka twente-thuu zakubadwa ameneyo, ndi kukamusiya iye uko ngati mtembo mnyumba yosungira mitembo? Ndipo angatenge khanda lofunikalo, mnofu wako womwe ndi magari? Ndipo nkumenyetsa pemphero lako pankhope yako yomwe? Ndiyeno iwe ukutanthauza kunena kuti iwe udzamatutumikira Iye?”

³⁶ Ine ndinali nditayima pakati pa malingaliro. Izo zinkayenera kugamulidwa. Kenako ine ndinayika dzanja langa pamutu wake wawung'ono, ine ndinati, “Ambuye anapereka, ndipo Ambuye atenga, lidalitsike Dzina la Ambuye!” Ine ndinamverera kupepukidwa.

³⁷ Ine ndinati, “Sharry, wokonedwa, Adadi sangapite kumene iwe uli tsopano, koma Adadi akhoza kudzabwera tsiku lina. Ine ndikakuyika iwe pa nkono wa Amayi, ndi kukuyika iwe mmanda, koma Adadi adzakuwonanso iwe tsiku lina.”

³⁸ Bambo Isler, amene mwinamwake akhala pano tsopano (ine sindikutha kuwona kudutsa mu khamuli), yemwe anali nduna yakale ya boma kuno la Indiana. Ine ndinali ndikuyenda mu

msewu waukulu. Bambo Isler, ine ndikuganiza inu mukukhoza kuzikumbukira bwino bwino zimenezo.

³⁹ Ine ndinali nditayika manja anga kumbuyo kwanga, ndikupita ku manda, kusefukira kwa madzi kutangotha, ndikulira. Ine ndinkakonda kupita kumeneko madzulo. Nkhunda yakale inkakhala mu mtengo, ndipo inkandiyimbira ine. Zinkawoneka ngati kupyola mu mphepo ya mapayini amenewo ndi mitengo, zinkawoneka ngati nyimboyo imanong'ona kudzera mmenemo, ikuti:

Kuli Dziko kutsidya kwa mtsinje,
Limene timalitcha kokoma kwanthawizonse,
Ife timangofikako ku gombelo mwa lamulo la
chikhulupiro;
Mmodzi ndi mmodzi ife tidzafika pa chipata,
Kumeneko kukakhala ndi achisavundi,
Tsikulina adzakayimba mabelu agolide
amenewo kwa inu ndi ine.

⁴⁰ Bambo Isler, akuyendetsa galimoto yawo yakale, analumphira panja, ndipo anadzayika nkono wawo mondikumbatira ine. Iye anati, “Ine ndakumva iwe ukulalikira pa ngodya ya msewu, Billy; ine ndakuwona iwe utayima mu kachisi; ine ndakumva iwe poyimba nyimbo; momwe iwe umamukwezera Khristu, chimene iwe unati Iye anali!” Anati, “Tsopano Iye watenga abambo ako, mchimwene wako, mkazi wako ndi mwana wako.” Anati, “Tsopano kodi Iye akutanthauza chiyani kwa iwe?”

⁴¹ Ine ndinati, “Bambo Isler, ngati Iye anganditumize ine ku madera a otayika, ine ndingakamukondebe Iye! Pakuti, tsiku lina, kumusi uko mu mthunzi wakale wa malasha, chinachake chinachitika pansa apa mu mtima mwanga, mwakuti palibe chimene chingafufute icho. Sichinali chirichonse chimene ine ndinachita. Chinali chisomo Chamuyaya cha Mulungu chimene chinandigwira ine mu ora la kusankha kwakukuluko!”

⁴² Ndipo pamene Ambuye wathu wodala, mu Getsemane, pamene ankapita kumeneko, pamene Iye ana-...kuti akakanidwe ku Yerusalemu, ndipo bungwelo linali loti likatenga moyo Wake, pamene kopita Kwamuyaya kwa moyo uliwonse, umene unayamba wakhalapo kapena udzakhale pa dziko lapansi, unkatsamira pa chigamulo Chake.

⁴³ Oh, momwe langa linaliri laling'ono, kuyerekeza ndi ilo! Momwe lanu linali laling'ono, poyerekeza ndi ilo! Zomvetsa chisoni kwambiri kuti ife sitimakhoza kupirira zinthu zazing'ono izi!

⁴⁴ Koma mu ora lalikulu lovuta lija, mpaka Iye anavutika, podziwa zinthu zonse, mpaka madzi ndi Mwazi zinalekanitsidwa mu thupi Lake, ndipo madontho aakulu a thukuta onga Magazi

anatsika kuchokera pa chipumi Chake. Iye anafa imfa yochuluka mu Getsemane kuposa momwe Iye anachitira pa mtanda.

⁴⁵ Iye anali basi basi pa chochitika cha izi, basi nkondo yaikulu isanayambe, ndipo Iye anatenga Mgonero. Iye anawasonkhanitsa ophunzira Ake pamodzi, kuti akambirane nawo zinthu.

⁴⁶ Ndipo umo ndi momwe Iye amachitira nanu inu ndi ine, basi nkondo yaikulu ya moyo isanayambike. Nkondo yaikulu ya chabwino ndi choyipa isanayambike kumenyedwa mkati mwathu, Mulungu amatibweretsa ife ku Getsemane. Iye amatibweretsa ife ku mgonero, ndipo Iye amakambirana nafe ife zonse.

⁴⁷ Uko mu Phoenix, Arizona, kunali atatu aang’ono omwe anakonda kundiyimbira ine, “Ine ndikufuna kukambirana ndi Yesu. Ndikufuna kunena kuti, ‘Yesu, Inu munandikonda ine pamene njira yanga inali yopapatiza kwambiri. Pamene kunali kwamdima kwambiri kulephera kuti ndikanawona patali, Inu munandikonda ine pamene kunali kwamdima.’” Ndipo nyimbo yaing’ono yimapitirira kumanena, kuti, “Ine ndikufuna kuti tikambirane izo.”

⁴⁸ Ndipo ndi chinthu chabwino kuti amuna ndi akazi a padziko lapansi, ayime paulendo wautali wamoyo, ndi kukambirana ndi Yesu, kukhala ndi mgonero ndi Iye, mu chiyanjano. Kenako nkondo imayamba, ya mayesero ndi kuyesa. “Mwana aliyense amene amabwera kwa Mulungu, amayenera kuyesedwa.”

⁴⁹ Tsopano, Mgonero si, sumaperekedwa ndi cholinga chimene ambiri amaganiza kuti chiri. Izo zimaphunzitsidwa ndi chipembedzo chinachake cha mpingo, kuti mgonero umatchedwa “miyambo yotsiriza,” kuti iwo umakhudza chipulumutso. Mgonero sukHUDZANA ndi chipulumutso. Mgonero sumakupatsani inu chipulumutso. Kaya inu muwutenga iwo mu imfa yanu, kapena—kapena chiyani, iwo ulibe kanthu kochita ndi chipulumutso chanu.

⁵⁰ Icho ndi chikumbutso. Yesu anati, mu Uthenga, Iye anati, “Izi muzichita mu chikumbutso cha Ine.” Osati, iwo ukutsamira kapena ukulozera ku chipulumutso, koma ndi mu chikumbutso cha ntchito yomalizidwa imene inachitika mwa inu, mwa Mzimu Woyera. Ndi chikumbutso.

⁵¹ Tsopano alipo ambiri amene amadya Mgonero sanapulumsidwe. Ambiri anadya nkHOSA ya pasaka ndipo anafera mchipululu. Ndipo ambiri amadya Mgonero, lero, amene sadzamuwona konse Mulungu.

⁵² Koma iwe sungakhale wolandira wa chipulumutso Chake ndipo osamuwona Iye, chifukwa chipulumutso ndi mphatso ya Mulungu. Ndipo Mgonero ndi chikumbutso cha Nsembe yayikulu, yokwanira zonse imene inapangidwira kwa chipulumutso chimenecho. Iwo ndi woti ulole anthu awone

kuti ife timakhulupirira mu imfa, kuyikidwa mmanda, ndi kuwuka kwa Ambuye Yesu Khristu. Iwo umayimira ntchito yomalizidwa.

⁵³ Chipulumutso kamodzi sichinamalizidwe, mu kupereka mbuzi, nkhosa, ng'ombe yamphongo, mu Chipangano Chakale, chifukwa magazi a Chipangano Chakale sankakhoza kutetezera tchimo. Iwo ankangokhoza kokha kuphimba tchimo. Iwo ankalozera ku nthawi imene izo ziti zidzamalizidwe. Mawa usiku tidzafika mkati mwake pa zimenezo. Koma icho chinali choyimira chabe.

⁵⁴ Koma pamene Yesu anabwera, ndipo Magazi Ake nakhetsedwa pa Kalvare, uko kunali kusudzulidwa kwathunthu kwa tchimo. Iwo anachotsera tchimo kutali. Iyo ndi njira yokhayo ya chipulumutso. Palibepo kujowina-tchalitchi, palibe makalata a chiyanjano, palibepo ubatizo wamwambo, palibepo Mgonero, kapena chirichonse mu mwambo, kapena chinthu chirichonse chimene chinasiyidwa ndi Mulungu, ngati zinthu zokhudzana ndi chipulumutso; izo zonse ndi chikumbutso cha ntchito yomalizidwa!

⁵⁵ Ubatizo wa mmadzi sumakupulumutsani inu, mochuluka monga momwe anthu nthawizina amaganizira kuti iwo umatero. Ubatizo wa mmadzi ndi chikumbutso cha imfa, kuyikidwa mmanda, ndi kuwuka cha Ambuye. Iwo sumakupulumutsani inu.

⁵⁶ Mgonero umakhala mu chikumbutso cha zowawa Zake zazikulu ndi kutuluka Kwake, ndi thupi Lake lonyemedwa, ndi Magazi Ake amene anakhetsedwa. Iwo si Magazi enieni, ilo si thupi lenilenilo; koma ndi mu chikumbutso cha thupi Lake lenileni, ndi Magazi Ake ofunika. Ndipo ife timachita izo ngati cholamulidwa, ndipo Yesu anatilamulira ife kuti tizichita izo. Malingana ngati Iye palibepo, ife tiyenera tizichita zimenezo.

⁵⁷ Ife tiri ndi chithunzi chachikulu, chokongola mu Bukhu, cha Kalata ya Ahebri, mu mutu wa 7. Ine ndikufuna kuti ndiwerenge malo aang'ono chabe mu Ahebri 7, kuti ndipeze nkhani yoti iyende ndi izi.

Pakuti Melkizedeki uyu, mfumu ya Salemu, wansembe wa Mulungu wammwambawamba, amene anakumana ndi Abrahamu akubwerera kuchokera kokapha mafumu, ndipo anamudalitsa iye;

Kwa amene mbadwa Abrahamu anampatsa chachikhumi...cha zonse; poyamba pokhala mwa kutanthauzira Mfumu ya chirungamo,...pambuyo pake Mfumu ya Salemu, yomwe ili, Mfumu ya mtendere;

⁵⁸ Zindikirani, ife tikufuna kuti tibwerere, ndi kukaganiza. Paulo apa akulozeranso kwa munthu wa Chipangano Chakale. Mu Bukhu la Genesis, ife tikutenga moyo wa Abrahamu, kuyambira mutu wa 12 wa Genesis. Mulungu

akumupatsa Abrahamu lonjezo, ndipo kudzera mwa Abrahamu pakanadzabwera Mbewu yolungama. Ndipo Abrahamu, monga zimakhulupiriridwa ndi ambiri kuti anali Myuda, iye sanali. Abrahamu anali wamitundu, Mkasidi wochokera ku mzinda wa Uri. Ndipo iye anadzakhala mtumiki wa Mulungu, osati chifukwa chakuti iye anali wosiyana ndi wina aliyense, koma chifukwa cha kusankha kwa Mulungu.

⁵⁹ Inu simunapulumsidwe chifukwa chakuti ndinu munthu wabwino. Inu munapulumsidwa chifukwa Khristu anakusankhani inu. Palibe munthu amene amamufunafuna Mulungu; Mulungu amamufunafuna munthu. Yesu anati, “Palibe munthu angabwere kwa Ine pokhapokha Atate Anga atamukoka iye poyamba.” Ndipo ngati ife tingayime kwa mphindi pang’ono ndi kuzindikira kufunikira kwakukulu kwa chinthu chimodzi chimenecho, kuti anali Mulungu Amene anakusankhani inu, osafuna kuti inu muwonongeke; koma anapereka kwa inu mwayi, ndipo anakuyitanani inu, ndipo anakusankhani inu kuti mudzakhale wantchito Wake. Chabwino, nchiyani chimene chingakhale chamtengo wapatali kuposa chimenecho? Popanda inu kukhala ndi chisankho! Izo zingakhale zosatheka kwathunthu kuti munthu aliyense amufunefune Mulungu, pakuti iye ali, mwachibadwa, ndi wochimwa, ndipo alibe kanthu mwa iye kotu kangapereke chikhumbo choti azimutumikira Mulungu.

⁶⁰ Kodi inu mungapite kwa nkumba ndi kukaiwuza iyo kuti ikulakwitsa? Iyo ndi nkumba, mwachibadwa. Kodi inu mungaiwuze iyo kuti zakudya zake ndi zolakwika? Ndithudi ayi. Mwachibadwa, iyo ndi nkumba. Inu mukuiwuza iyo kuti ikanakhala mwanawankhosa, koma iyo imakhala yokhutsidwa ngati nkumba.

Ndipo wochimwa amakhutsidwa ngati wochimwa, chifukwa chikhalidwe chake ndi wochimwa.

⁶¹ Ndipo ndi izi apa! “Ife tonse tinabadwa mu tchimo, tinawumbidwa mu kusaweruzika, tinabwera ku dziko tikuyankhula mabodza;” mwachibadwa, mwana wa kusamvera, wopanda Mulungu, wopanda chiyembekezo, mkwiyo wa Mulungu ukukhala pa ife. Ndipo mwa chisomo cha chikondi cha Khristu, Mulungu, mu chisomo Chake cha yekha ndi umphamvuzonse Wake, amagogoda pa mtima wanu ndi kudzakupatsani inu mwayi wodala, ndi kukutembenezani inu, ndi kukutumizani inu panjirapo. Kodi mungazikane bwanji zimenezo? Amasintha chikhumbo chanu chonse, amakutembenezani inu, ndi kukuyambitsani inu njira inayo! Oh, inu mudzakhala wopusa, kwa dziko; koma inu mudzakhala wodalitsika, pamaso pa Mulungu. “Odala ali iwo amene amva njala ndi ludzu la chirungamo, pakuti iwo azadzazidwa,” anatero Ambuye wathu Yesu Khristu. Mulungu, mwa chisomo Chake chodabwitsa!

⁶² Zindikirani, icho chinali chimene Mulungu anachita, chimene Mulungu anachiyitana. Inu munalibe khumbo loti muyitane. Inu simukanakhala ndi khumbo loti muyitane, chifukwa chikhalidwe chanu chinali chosiyana kwathunthu ndi Icho. Koma Mulungu, mwa kusankha, anakuyitanani inu ndipo anakutembuzani inu, ndipo anakazikitsa zokonda zanu kwa Khristu ndi zinthu za Kumwamba. Ife tingakhoze bwanji kuchikana Icho?

⁶³ Kenako Mulungu anasonyeza, mwa Abrahamu, chimene Iye akanati adzawachite onse. Sikuti lonjezo lodala ili la chiwukitsiro ndi Moyo Wamuyaya linangoperekedwa kwa Abrahamu yekha, koma kwa Mbewu yake ya pambuyo pake, Oyitanidwawo, Osankhidwa a Mulungu.

⁶⁴ Ndipo ife tikuzindikira kuti, Abrahamu uko mminda kumene iye anali mwendamnjira. M'bale wake, iye ankamutcha iye, Loti; iye analidi mdzukululu wake, mwana wa mchimwene wake. Ndipo nthawi inafika ya kuyesedwa. Ndipo Loti anafowoketsedwa ndi kuyesedwako. Iye ndi chithunzi changwirowo cha wokhulupirira wachithupithupi lero. Pamene mayesero anabwera, kuti akhale pa dziko lowuma, Abrahamu anamupatsa iye kuti asankhe. Ndipo Loti anatumula maso ake ndipo anawona minda, chigwa, ndipo munali modzadza ndi udzu. Munalinso modzadza nyumba zabwino. Munali modzadza ndi chisangalalo. Munalinso modzadza ndi tchimo. Koma Loti, pokhala wachikhalidwe cha chithupithupi, wokonda dziko la tsopano lino kuposa zinthu ziri nkudza, anasankha makamaka kukhala moyo wapamwamba m'moyo uno, kuposa kudzakhala ndi Moyo ukatha uno.

⁶⁵ Abrahamu, choyimira changwirowo cha wokhulupirira woona amene anatsukidwa mu Magazi a Mwanawankhosa, amene zokhumba zake zinakhazikitsidwa pa zinthu zakumwamba, anati, "Ine nditenga njira ndi onyozeka ochepa a Ambuye. Mosalabadira kuti izo zindichotsera kutchuka kwanga, chirichonse chomwe icho chingatengere, ine nditenga njira ndi ochepa a Ambuye." Ndipo iye anasankha kukhala mdziko limene Mulungu anakamuyikako iye, pansu pa nthawi yoyesedwa.

⁶⁶ Ine ndikudabwa usikuuno ngati ndikuyankhula kwa anthu omwe anayambapo kuti azipitirira ndi Mulungu, ndipo, pamene nthawi yoyesedwa inafika, inu munasankha kubwerera ku dziko ndi kumakachita zinthu za mdziko, kapena kodi inu munatenga njira yakale yolimba ya chipulumutso?

⁶⁷ Kodi inu munachita monga Mose, pamene iye anali pansu pa kuyesedwa, pamene iye anayika phazi lake pa mpando wachifumu wa Igupto? "Koma, iye anachiyesa chuma cha Khristu kukhala chuma chachikulu kuposa chuma chonse cha Igupto." Iye anasiya Igupto, sankasamala ndi golide wochuluka bwanji, ndi kutchuka kungati. . . Iye anamutenga Mulungu pa

Mawu Ake ndipo anasiya zinthu zaku Igupto, akuwerengera chitonzo cha Khristu kukhala chuma choposa chuma cha Igupto.

⁶⁸ Kodi ife timachita chiyani pansi pa kuyesedwa, pamene mayesero ovuta abwera? Pamene iwo anena kuti chifukwa chakuti inu mwadzilekanitsa nokha ku zinthu za mdziko, ndiye kuti ndinu wotentheka wachipembedzo, kodi kupanikizika kumabwera? Iko kumayenera kubwera, ndipo inu mukuyenera kupanga chisankho.

⁶⁹ Koma ine ndikanakonda ndikhale pansi pa mithunzi ya Wamphamvuzonse, ine ndikanakonda nditatenga njira yanga ndipo, monga Yakobo, ndikhale ndi mtsamiro wamwala. Ine ndikanakonda ndikanamatengedwa ndi dziko lapansi ngati, “chidempete,” kuposa kukhala ndi chuma chonse ndi madalitso amene dziko lino lingakwanitse kuwapereka. Chifukwa, ochuluka ndi madalitso a Mulungu kuposa chuma chonse ndi golide ndi siliva za dziko lapansi lino! Tsopano zindikirani.

⁷⁰ Ndiye pamene mayesero aakulu anabwera, Loti anapita pansi mu tchimo. Kumbukirani, iye anapita kuchokera ku phiri, anatsikira ku chigwa. Iye anabwerera mmbuyo, monga . . . Choyimira changwiwo cha Chikhristu chachithupithupi lero, chotchedwa, anasankha kutenga njira yophweka, bedi lamaluwa lophweka, kuposa kukhala woona mu nthawi ya mayesero. Ndipo potsiriza iye analowa mmavuto.

⁷¹ Ndipo inu mudzatero, nanunso. Pamene inu mudzasankha bedi lija lanthenga lophweka, kumbukirani, inu mudzakhala pa mavuto, chinachake. “Machimo anu adzakupezani inu!” Ndipo Mulungu adzakupezani inu, tsiku lina.

⁷² Ndipo tsiku lina mfumu, mafumu Amitundu aku zigawo zazikulu kutali, anadzabweramo ndipo anamutenga Loti ndi ana ake, mkazi wake ndi zonse zimene iye anali nazo, ndipo anathawa nawo iwo.

⁷³ Ndipo tsiku lina, mzanga wofooka, ngati iwe sukhala pansi pa Magazi, maufumu a Satana adzakupeza iwe ndi kukutengera iwe kutali, ngati iwe sukhala pansi pa Magazi.

⁷⁴ Ndipo Abrahamu, woyimira wa olungama, iye anali wokhudzika kwambiri ndi mdzukulu wake, woyimira wa chenichenicho, Mkristu woona amene wayesedwa ndi kuyesedwa, ndipo watsimikiziridwa.

⁷⁵ Tsopano, akaziwo anali ndi zambiri zoti achite nazo izo. Mkazi wa Loti anali wachithupithupi, wachithupithupi kwambiri. Iye akuima lero mminda uko, ngati chulu cha mchere, ngati chamanyazi, kwa iwo odutsapo.

⁷⁶ Sarah, mkazi wokongola, ankafuna kuchita chimene Mulungu ankafuna kuti iye achite. Iye ankamulemekeza mwamuna wake; monga, ife tinayankhula motsimikiza kwambiri pa zimenezo usiku wathawu. Ndipo iye anakhala

ndi Abrahamu, mosalabadira chimene chingabwere kapena kupita. Iye anakhala ndi iye chifukwa iye anakhala ndi lonjezo. Ndicho chinthucho.

⁷⁷ Ndiye pamene Loti anatengedwa, mtima wa Abrahamu unamutsatira iye. Ndipo iye anasonkhanitsa gulu la ankhondo la akapolo ake omwe, ndipo anamutsatira m'bale wake. Ndipo choyimira chokongola kwambiri. Iwo anatenga malupanga awo ndipo anawasadza mafumu amenewo, mpaka panalibe mmodzi wa iwo amene anatsalira.

⁷⁸ Ndipo ndicho choyimira cha mlaliki wa Uthenga, pamene iye awona kuti tchimo lagwira mpingo wake ndi kuwagwira anthu. Iye amatenga Uthenga wodala wakale, Lupanga la Mzimu, ndipo iye amalisadza ilo ndi kulisadza ilo, mpaka iye atalidulapo tchimolo mu mpingo wake, ngati iye ali wantchito woona wa Mulungu. Iye amachotsa zamkutu zonse, zolongolola, zamiseche. Iye amachotsa zinthu zonse ndi zikhalidwe zachithupithupi za mdziko zomwe zakwawira mu mpingo, ngati iye ali mtumiki woona wa Mulungu. Iye amatenga Mawu, ndi kuzisadzula izo kuzichotsa ku mbali imodzi kupita ku imzake, mpaka iye atadulapo chirichonse.

⁷⁹ Ndipo kenako pamene iye anamutenga Loti, m'bale wake wobwerera mmbuyo, ndi ana, ndipo iye ankawabweretsanso iwo ku kuyanjanitsidwa, zindikirani, Mfumu yaikulu iyi inabwera kuchokera ku Yerusalemu, ndipo inakumana naye iye. Melkizedeki! Kodi ameneyo anali Munthu wantundu wanji? Iye ankatchedwa “Mfumu ya Salemu.” Chimene, wophunzira aliyense amadziwa kuti *Salemu* anali “Yerusalemu.” Iye ankatchedwa Salemu iye asanatchedwe Yerusalemu. Kodi munthu uyu anali ndani yemwe anakumana naye iye, yemwe ankaganiza kuti iye anali atatenga sitepe yoyenera? Kodi Munthu uyu amene anayima pafupi naye anali ndani? Penyani Yemwe Iye ali.

. . .Iye ndi *Mfumu ya Yerusalemu*, ndipo Iye alinso *Mfumu ya Mtendere*;

Ndime yachitatu:

*Wopanda bambo, wopanda mayi, wopanda abale
wopanda chiyambi cha masiku, kapena wopanda
mathero a moyo; . . .*

Kodi Kalonga wamkulu uyu anali ndani yemwe anakumana naye nk'hondo itatha? Tiyeni titembenuzire ku Genesis, ndime ya 14 . . . mutu wa 14 ndi ndime ya 18.

*Ndipo Melkizedeki mfumu ya Salemu anabweretsa
mkate ndi vinyo: . . .*

*. . . anadalitsa izo, ndipo anati, Wodalitsika akhale . . .
Mulungu wammwambamwamba, wosunga wa miyamba*

ndi dziko lapansi: ndipo wodala akhale Abrahamu yemwe ali wantchito Wake.

⁸⁰ Nkhondoyo itatha, chigonjetso chitapambanidwa, kuyeretisa kutatha kuchitika, Melkizedeki anakumana ndi Abrahamu mu zidikha, ndipo anabweretsa mkate ndi vinyo, ndipo anapereka iwo kwa iye.

Ndipo Ndani? Ameneyo sanali wina kuposa Mmodzi amene anakumana ndi Abrahamu pafupifupi chaka mtsogolo, anakhala panso pa mtengo ndi kumayankhulana naye iye.

⁸¹ Ndipo Melkizedeki yemweyu uyu anati, “Ine sindidzatenganso za chipatso cha mpesa mpaka ine ndidzamwe icho mwatsopano ndi iwe, mu Ufumu wa Atate Anga, nkhondoyo ikadzatha, pamene chigonjetso chapambanidwa.” Ndiye ife tidzatenga izo mwatsopano mu Ufumu Wake, pamene nkhondo yotsiriza idzamenyedwa. Pamene lupanga lotsiriza lapha choyipa chotsiriza cha dziko lapansi, ndipo Mpingo waukulu wa Mulungu wamoyo walakika, Khristu adzakumana nawo iwo mu mlengalenga, ali ndi mkate ndi vinyo, kachiwiri, ndipo adzakhala ndi Mgonero, ndi kwa Muyaya mu Kukhalapo kwa Atate.

⁸² Oh, mwendamnjira wotopa, usikuuno, bwerera ku Nyumba ya Atate. Tulukani mu Sodomu! Inu mwayanjanitsidwa ndi Magazi. Ndipo usiku waulemelo wachikumbutso uwu, pamene Melkizedeki wathu wamkulu, Amene analibe chiyambi cha masiku kapena mathero a moyo, koma ndi Mfumu ndi Kalonga kwanthawi za nthawi.

⁸³ Mzimu Woyera pano usikuuno ukukopa osapulumsidwawo, tsopano ngati inu muli opanda Khristu usikuuno. Ndipo pamene nkhondo idzatha, ngati inu mukufuna kuti mudzakumane naye Iye mu mtendere ndi kudzadya Mgonero ndi Iye, ndipo inu mwalonjeza kuti inu mumamukonda Iye, ndipo mwadzilekanitsa nokha ku zinthu za mdziko. Tengani Uthenga wakale wolimba ndi njira yachikale yolimba, ndipo mumwe chikho cha kuwawa kwa mazunzo a dziko lapansi, ndi kumwa mankhwala akhambi a mazunzo a mdziko lapansi; zapatsidwa kwa ife ndi Baibulo kuti tidzamwa vinyo wokoma wa Kumwamba tsiku lina, pamene ife tidzakumana naye Iye mu mtendere uko pakati pa Miyamba ndi dziko lapansi, pamene Iye akubwera kudzapereka Mgonero. [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi].

⁸⁴ Mulole mitima yathu iziganizire izi, “Ine ndidzamwa icho mwatsopano ndi inu, mu Ufumu wa Atate Anga.” Ngati Iye angabwere Isitara ina isanabwere, ngati inu mungafe Isitara ina isanafike, izo sizidzalepheretsa chochitika chachikulu chimenecho. Pakuti ine ndikuti, mwa Mawu a Ambuye, kuti iwo amene akugona mwa Khristu adzatulukira poyamba. Ndipo ife amene tiri moyofe ndipo tatsalira tidzakwatulidwa

limodzi nawo, pamodzi, mu mlengalenga, kukakumana ndi Ambuye. Ndipo Melkizedeki wamkulu wa Kumwamba, Mfumu ya osati Yerusalemu wathupi, koma Mfumu ya Yerusalemu Wakumwamba, Yerusalemu Watsopano, adzakumana nafe ife, ndipo tidzapatsidwanso kachiwiri vinyo ndi mkate.

⁸⁵ Usikuuno ife ndi oti titenge ziphiphiritso za izi. Ife ndi oti tizichita izo mpaka ife tidzamupeze Iye akubwera kachiwiri. Mulole ife tidzapezeke okhulupirika pamene ife tikuweramitsa mitu yathu mphindi chabe, kwa mawu a pemphero.

⁸⁶ Aliyense mwakachetechete basi momwe mungathere, mu mphindi yaulemu kwambiri iyi, yoyera. Ndi mophweka bwanji momwe zinthu izi zingatipulumukire! Baibulo linati, “Kuwopa kuti zinthu zimenezo zingatipulumuke, ndi kunyalanyaza chipulumutso chachikulu chotero.” Ndi zophweka kwambiri kuziyiwala izo. Ife sitimabwera ku tchalitchi kuti tidzawonedwe. Ife sitimabwera kuti tidzamve kuyimba kwabwino kapena ulaliki wabwino. Ife timabwera ku tchalitchi kuti tidzampembedze, kuti tidzampembedze Mulungu.

⁸⁷ Ndipo mmodzi aliyense wa ife, matupi athu achivundi ali ndi solo yomwe iti idzakumane ndi Iye tsiku lina. Ndipo mu kukonzekera kubwera kwa tsiku lalikulu la kupachikidwa ili, mu chikumbutso cha kuchoka Kwake, usikuuno, ngati inu simuli Mkhristu, simunamulandirepo Khristu mmoyo wanu ngati Mpulumutsi, kodi inu mwakhutitsidwa mokwanira ndi kulalikira kwa Mawu, ndipo kodi Mzimu Woyera wayima pafupi ndi inu kuti unene kuti, “Ndinu wolakwa. Tsopano tembenukani ndipo muyambe njira inayo?” Kodi mungalengeze chomwecho pokweza dzanja lanu, kuti, “M’bale Branham mundipempherere ine. Ine tsopano ndikupempha mapemphero anu kuti Mulungu andichitire ine chifundo?” [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi]. Kodi inu mungakweze dzanja lanu pamene ife tikuyembekezera? Mulungu akudalitseni inu, bwana. Wina wakenso?

Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu, bwana. Mulungu akudalitse iwe, wamng’ono. Mulungu akudalitseni inu. Kodi wina...? Mulungu akudalitseni inu, dona.

⁸⁸ Inu mukuti, “M’bale Branham kodi izo zikutanthauza chirichonse kuti ndikweze dzanja langa?” Basi kusiyana kwa pakati pa imfa ndi Moyo. Chachikulu kuposa Moyo ndi chiyani? Inu mumakonda...inu mukayang’ana pa chirengedwe. Inu mumachikonda icho; inu mumadana nazo kuti muchoke kwa icho.

⁸⁹ Kutsidya kwa msewu, kuno, pamene mkazi wa mchimwene wanga ankafa, mmawa wina zaka zambiri zapitazo, pamene Ruth wamng’ono wosauka anadzutsa mutu wake, ndipo

apo panali phwiti atakhala mu mtengo wa nthudza, ndipo iye ankafuna kuti amuwone iye kenanso... Momwe iye anakondera chirengedwe. Koma tsiku lina pamene Yesu adzabwera, iye adzamva mbalame za Muyaya zikuyimba. Maluwa osafa adzakhala akukula. Sikudzakhala matenda, chisoni, kapena imfa, chifukwa iye anapanga mtendere wake ndi Mulungu ndipo anamulandira Khristu wamkulu Amene anamufera iye. Ndi chitsimikizo chodala ichi Amene sangalephere, Mawu odala a Mulungu Amene sanganame, analonjeza Moyo Wamuyaya kwa iwo amene anakhulupirira. Pamene inu mukweza dzanja lanu, izo zimasonyezera kuti mzimu mkati mwanu wapanga chisankho. Mulungu akudalitseni inu, dona.

⁹⁰ Chinachake mwa inu, a—mzimu... Mwa chibadwa mikono yanu inapangidwa kuti izilendewera pansu, ndipo pamene inu mukweza dzanja lanu inu mumanyoza malamulo kumene a mphamvu yokokera pansu. Izo zikuyenera kukhala zauzimu. Ndi—ndi zotsutsana ndi sayansi... zotsutsana ndi zinthu zonse zasayansi kuti inu muphwaye malamulo a mphamvu yokokera pansu. Izo sizingakhoze kuchitidwa pokhapokha patakhala chinachake chauzimu. Mikono yanu ikhoza kumalendewerabe pansu mopitirira. Koma ngati, mu mtima mwanu, inu mukukhulupirira nkhanu ya Uthenga ndipo mwapanga chisankho chanu usiku uno, kuti mwathana nalo tchimo, ndipo pa njira yokongola iyi ya ku Kalvare pamene mawa, pa firii koloko, mu chikumbutso, ife tidzakondwerera tsiku limene Yesu anafera chipulumutso chanu... Ndipo inu munaganiza mokwanira za izo ndipo Mzimu Woyera wabwera ndipo wadzagogoda pa mtima panu ndipo tsopano inu mwalandira icho... .

⁹¹ Inu basi... chinachake mu mtima mwanu chikuti, “Kweza dzanja lako.” Izo zimasonyezera kwa anthu, ndi kwa Mulungu, kuti inu mukukhulupirira izo ndipo mukuvomereza izo. Mulungu akudalitseni inu, ana aang’ono nonsenu: atatu kapena anayi a iwo pano pa guwa, anyamata ndi atsikana pafupifupi eyiti, usinkhu wa zaka teni, iwo onse anakweza manja awo nthawi ina. Yesu anati, “Lolani ana adze kwa ine. Musawaletse iwo, pakuti Ufumu uli wotere.” Kodi alipo wina ife tisanapemphere?

⁹² Mulungu akudalitseni inu, dona. Izo ndi zenizeni... Inu mukhoza kukhala kuti mwachitapo zinthu zambiri, dona, mmoyo. Izo zinali zenizeni; ine ndikukukhulupirirani inu kukhala a—mkazi woonamtima. Ndipo kumbukirani, inu sibwenzi mutakweza dzanja lanu, mlongo wokondedwa, pokhapokha chinachake mkati mwanu, chinachake pansu mwa inu chikanati, “Chita zimenezo.” Izo zikhoza kuwoneka zopusa pang’ono tsopano kwa malingaliro achithupithupi, koma m’bale, pa tsiku limenero pamene dokotala adzachoka pakhomo

ndi kudzanena kuti, “Izo zatha.” Pamene iye adzachoka pa galimoto lophwanyikalo ndi kudzakokera kunja thupi lanu laling’onolo, magari akutayika ndipo mtima wanu uli wefufu, “Palibe chifukwa chopusitsana ndi iwo; iwo apita.” Oh, mai. Ndipo monjenjemera mu ora limodzi inu mudzayesera kuti mulape, ndipo Mulungu anati, “Mu matsoka anu Ine ndikhoza kungoseka.” Koma pamene inu mukukhala m’malinaliro anu abwino, pamene inu. . . [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi].

⁹³ Atate, pamene tikuwubweretsa uthenga uwu kotseka, ndi zokolola za anthu pafupifupi fifitini, akweza manja awo, omwe akhala ali ochimwa miyoyo yawo yonse. Ndipo tsopano, mwa chisomo, Inu mwayankhula nawo iwo, mwawatembenusa iwo mozungulira ndipo mwawalola iwo ayang’anizane ndi Kalvare, ndipo akumva Mawu amenewo kuchokera pa milomo ya Mwana wa Mulungu, “Atate, akhululukireni iwo, iwo samadziwa chimene iwo amachita.” Koma usikuuno iwo alandira Uthenga. Ife tikumumva Iye akunena, masiku angapo izi zisanachitike, “Iye amene amva Mawu Anga, ndi kukhulupirira pa Iye amene anandituma Ine, ali nawo Moyo wosatha; ndipo sadzabwera mu chiweruzo, koma wadutsa kuchoka ku imfa wapita ku Moyo.” [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi].

⁹⁴ Ife tikuwapereka iwo kwa Inu usikuuno, Ambuye, ngati ana Anu. Mulole madalitso Anu Amuyaya akhale pa iwo, mu Dzina la Khristu ife tikupemphera. Mulole iwo abwere Lamlungu mmawa, atanyamula zovala zawo, akuti, “Ine ndikufuna kuti ndipange kuvomereza kwapoyera kwa dziko lino, kuti ine ndine wokhulupirira. Ine tsopano ndikukhumba kuti ndibatizidwe mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu; kuyitana pa Iye kuti andidzaze ine ndi Mzimu Woyera, ndi kundisamalira ine kudutsa m’moyo.”

⁹⁵ Adalitseni akazi achichepere awa, amuna achichepere awa, okalamba, ana achichepere, ndi onse, asalalireni iwo, Atate, iwo ndi Anu. Ndipo mu zipatso za uthenga uwu usikuuno, ine ndikuwapereka iwo kwa Inu, monga zikhumbo. Ndipo iwo ali mdzanja Lanu, ngati mphantso zachikondi zochokera kwa Mulungu, Atate. Ine ndikupemphera kuti Inu muwasamalire iwo kudutsa m’moyo. Mu Dzina la Yesu ine ndikupemphera. Amenii. . .? . . .

⁹⁶ Ife ndife okondwa kukhala nanu kuno usikuuno, ndipo ife ndi okondwa kuti inu munabwera. Ndipo mawa usiku, Uthenga wathu ndi, mawa usiku, pa: *Ungwiro Wa Wokhulupirira*. Ndipo tsopano mudzabwere, mudzam’bweretse winawake ndi inu, ngati tchalitchi chanu chomwe sichidzakhala ndi misonkhano.

⁹⁷ Ndipo tsopano ife tikhala ndi Mgonero. Mwinamwake ena a inu. . . Ine basi ndangochedwa pang’ono, maminiti pang’ono, ndipo ife tiwabalalitsa iwo amene akuyenera kuti azipita.

⁹⁸ Ndipo iwo amene akufuna kuti atsaliwe kuti adye Mgonero ndi Kutsukana mapazi ndi ife, ife timakhulupirira mu kuchita

mwamtheradi chirichonse chimene Yesu anatsiyira kuti ife tizichita. Ndipo ngati Iye adzabwere mu kam'badwo kanga, ndi kudzandilola ine kuti ndidzakhale wabwinobwino mmalingaliro anga ndi kusunga chikondi Chake mu mtima mwanga, Ine ndidzakhala ndikuyetsetsa mwa kuthekera kwanga kuti ndizichita chirichonse cha izo, ndi kudzapezeka wokhulupirika pa malopo. Mulungu akudalitseni inu tsopano. 🕊

57-0418 Mgonero
Branham Tabernacle
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©2024 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

www.branham.org